so anafa.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anasiyana ndi Mulungu, anthu onse nawonso anasiyana ndi Mulungu.

-Mulungu ndi woyera.
-Mulungu sangathe kukhala ndi tchimo.
-Chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa.



PHUNZIRO LA 13

1. Adamu ndi Hava anayesa kubisala kwa Mulungu. Kodi pali amene angathe kum'bisala Mulungu?
-Ayi.
-Mulungu amakuwona kulikonse kumene ife tamapita kapena tingapite.

2. Kodi Mulungu anamuyitana Adamu chifukwa chakuti Iye sankadziŵa kumene anali?
-Ayi

3. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuyitana Adamu?
-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye kuti alape machimo ake.
-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti sanamumvere Mulunguyo.
-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti anamumvera Satana.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi oyenera kumuyitana Adamu ndi anthu onse?

-Chifukwa chakuti Iye ndi amene anamulenga Adamu pamodzi ndi anthu onse.
-Chifukwa chakuti Adamu pamodzi ndi anthu onse ndi a Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu anamulenga Adamu pamodzi ndi anthu onse kuti adzimumvera Mulunguyo.

5. Kodi Mulungu anayilanga bwanji njoka?
-Tsopano njoka imakwawa ndi mimba yake.

6. Kodi Mulungu anamulanga bwanji Hava?
-Adzidzamva kupweteka kwambiri pobereka ana ake.

7. Kodi Mulungu anamulanga bwanji Adamu?
-Adamu adzidzalima pa dothi mpaka kutulutsa thukuta lambiri koma adzidzakolora zokolola za pang'ono.

8. Kodi zizindikiro zakuti Mulungu analitemberera dziko la pasi ndi zotani?
-Kuli minga ndi tchire lambiri.
-Kuli zipha zambiri ndi njoka.
-Kuli njala ndi kusefukira kwambiri kwa madzi.
-Nyama zimaluma anthu.
-Anthu ayenera kugwira ntchito molimbikira kuti apeze zakudya.
-Anthu amadwala.
-Anthu amafa.

9. -Nthaŵi yomweyo Mulungu atapereka chilango kwa Adamu ndi Hava, kodi Iye anapereka lonjezo lakuti adzatumiza ndani?
-Lakuti adzatumiza Mpulumutsi.

10. Kodi Mpulumutsi ameneyo adzakhala ndani?
-Adzakhala mwana wa mamuna wa m'namwali.

11. Kodi Mpulumutsiyo adzachita chiyani?
-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo.
-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya imfa.
-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya Satana.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu analonjeza zotumiza Mpulumutsi?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu onse kwambiri.



ra mbali zonse, kutchinjiliza Mtengo Wopereka Moyo uja, kuti wina asawuŵandikire.

-Mulungu atamuchotsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni, Iye anayika mngelo otchedwa akerubi cha kuvuma kwa mundawo ndi lupanga la moto pa chipata cha mundawo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anachita zimenezo?
-Chifukwa chakuti Mulungu samkafuna kuti Adamu ndi Hava abwererenso ku munda wa Edeni uja.

-Adamu ndi Hava sanakatha kubwereranso ku munda wa Edeni uja.

-Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu ndipo analakwa.

-Kodi Adamu ndi Hava anafa?
-Inde.

-Kodi Adamu ndi Hava anafa bwanji?

-Adamu ndi Hava anasiyana ndi Mulungu.
-Adamu ndi Hava anasiyana ndi Mulungu amene anaŵapatsa moyo.

-Adamu ndi Hava sanakathanso kukhala ndi Mulungu.
-Adamu ndi Hava sanakathanso kuyenda ndi Mulungu.

-Adamu ndi Hava amayenera kukhala mosiyana ndi Mulungu.

-Mulungu ndi woyera.
-Mulungu sangathe kukhala ndi tchimo.
-Chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa.

-Chifukwa chakuti Adamu di Hava anafa, anthu onse nawon-

Tiyeni teŵerenge Genesesi 3:22-23

22-Ambuye Mulungu anati, “Tsopano munthuyu ali ngati m’mene tilili Ife, pakuti akuzidziwa zinthu zabwino ndi zoyipa. Tisamupatsenso mwayi wakuti adzidya zipatso kuchokera mu Mtengo Wopereka Moyo, ndi kukhala ndi moyo mpaka kalekale.”

23-Chomcho Ambuye Mulungu anamuchotsa munthuyo m’munda mwa Edeni muja, kuti adzikalima mu dothi limene anamuwumbilalo.

-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi), ndi Mulungu Mzimu Woyera amkakambirana za Adamu ndi Hava.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkazidziwa zinthu zabwino zokhazokha.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkazidziwa zinthu zoyipa.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkakudziwa kumvera kokhakokha.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkakudziwa kusamvera.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava samkaŵadziwa manyazi.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkaŵadziwa manyazi.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkawudziwa moyo okha.
-Tsopano, Adamu ndi Hava amkayidziwa imfa.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, Mulungu anaŵachotsa m’munda mwa Edeni.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:24

24-Mulungu atamuchotsa munthu uja m’munda muja, anaŵayika angelo (akerubi) cha kuvuma kwa mundawo kuti adzilondela. Anayikaso lupanga la moto limene limkazunguli-



13. Kodi Adamu ndi Hava anali oyenera kulandira chikondi cha Mulungu?
-Iyayi. Anali oyenere kulandira imfa yosatha.

14. Kodi makolo oyamba a anthu onse anali ndani?
-Adamu ndi Hava.

-Kodi Adamu ndi Hava anachita chiyani atamulakwira Mulungu?
-Anazipangira okha zovala za masamba.

-Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava anazipangira okha zovala za masamba?
-Chifukwa chakuti amkayesayesa kubisa tchimo lawo.

-Kodi pali amene angathe kubisa tchimo lake kwa Mulungu?
-Palibe.

-Palibe amene angathe kubisa tchimo lake kwa Mulungu.

-Koma Mulungu anazikana zovala zimene Adamu ndi Hava anazipangira okha.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anazikana zovala zimene Adamu ndi Hava anazipangira okha?

-Kodi Mulungu samaŵakonda masamba?
-Iyayi.

-Mulungu ndi amene analenga masamba.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anazikana zovala za masamba zimene Adamu ndi Hava anazipangira okha?
-Mulungu amkafuna kumphunzitsa Adamu ndi Hava kuti palibe chimene iwo angachite kuti akhale oloredwa kwa Mulungu.

-Kodi tingazipange tokha kukhala oloredwa kwa Mulungu chifukwa cha zovala zimene tavala?
-Iyayi.

-Kodi tingazipange tokha kukhala aloredwa kwa Mulungu chifukwa cha ntchito zathu zabwino?
-Iyayi.

-Mulungu sadzaŵalora anthu amene amatsata njira zawo.
-Mulungu sadzaŵalora anthu amene amasankha njira zawo.

-Kodi ndi ndani yekha amene anali oyenera kumupanga Adamu ndi Hava kukhala oloredwa kwa Mulungu?
-Mulungu.

-Kodi Mulungu anamuchitira chiyani Adamu ndi Hava?

Tiyeni teŵerenge Genesesi 3:21

21-Ambuye Mulungu anamupangira zovala za zikopa za nyama Adamu ndi mkazi wake ndipo anaŵaveka iwowo.

-Mulungu anamupangira Adamu ndi Hava zovala za zikopa za nyama.

-Kodi Mulungu anazitenga kuti zikopa za nyamazo?
-Mulungu anapha nyama ndi kukusa zikopa zake.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapha nyama?

-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti kusamvera kumabweretsa imfa.
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti tchimo limabweretsa imfa.



-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti chilango cha tchimo ndi imfa.

-Imfa yoyamba ya thupi pa dziko la pasi ndi imfa imene Mulungu anapha nyama.

-Ngakhale kuti kusamvera kwa Adamu ndi Hava kumkayenera kulandila imfa, Mulungu anaŵaveka iwowo ndi zovala zimene Iye anapanga.

-Mulungu anamuveka Adamu ndi Hava ndi zovala zimene Iye anapanga chifukwa chakuti amkaŵakonda kwambiri.

-Adamu ndi Hava sanavale okha zovalazo.
-Mulungu ndi amene anamuveka Adamu ndi Hava zovalazo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanamulole Adamu ndi Hava kuti avale okha zovalazo?

-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti ndi Mulungu yekha amene angathe kuwaveka anthu.

-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti sadzaŵalola anthu amene amatsata njira zawo.

-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti sadzaŵalola anthu amene amasankha njira zawo.

-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti adzitsata njira ya Mulungu yekha.
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti adzisankha njira ya Mulungu yekha.

-Kodi Mulungu anapanga chiyani atatha kumuveka Adamu ndi Hava?